**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE**


NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

# NYENGO MSABATAYI

## KUYAMBIRA PA 30 MARCH MPAKA PA 5 APRIL, 2026

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI


Kuyambira lolemba mpaka lachitatu pa 1 April 2026, tiyembekezere nyengo **ya mvula ya mabingu m'madera ochepa yomwe idzigwa ya mphamvu** maka m'madera a m'phepete mwa nyanja ya Malawi kamba ka mphepo zosakhazikika zochokera kumvuma. Koma Pofika lachinayi Mphepozi zidzakhala zikukumana ndi zina zochokera kumwera chakumvuma ndipo izi zidzapangitsa madera ambiri kukhala ndi nyengo ya mphepo, yozizira komanso mvula yomwe ikuyembekezereka kugwa yamphamvu m'madera ambali mwa Nyanja ya Malawi monga **Nkhotakota, NkhataBay, Karonga**.




*Ulosi wamvula kuphatikiza masiku onse musabatayi.*

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo yamitambo yapatali patali madera ambiri komanso mvula yomwe inagwa yamabingu ndi yamphamvu maka m'madera akumpoto ndi kumwera. Mvula yambiri m'maola 24 yomwe tinalandira kuchokera kumwera inali ya mlingo wa **155.8mm kuchokera ku Kabalelyamayolo m'boma la Karonga pa 22 March, 2026.**




*Mapu akuonetsa mvula yochuluka yomwe talandira mu sabatayi kuyambira pa 23 mpaka 29 March 2026*

## LANGIZO M'SABATAYI:

**Mphepo ya mwera idziomba nthawi zina pa Nyanja ya Malawi.** Choncho onse ogwiritsa ntchito nyanja akhale osamala pofuna kupewa ngozi.

***For further information please contact:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatsindikizidwa Lamulungu pa 29 March, 2026.**